

# UTHENGA WABWINO

## WA CHOONADI

Malangizo ndi Chilimbikitso  
kuchokera m'Baibulo kupita kwa  
amene akulalikira Uthenga Wabwino

### KUWULULA ZA UTATU WA MULUNGU

(Nkhani ili mmunsiyi ikukamba za zimene zinalembedwa mu Mateyu 3:13-17, Yohane 1:31-34).

Pamene makamu a Ayuda anaimirira ndi kuyang'ana, Yesu analowa mu mtsinje wa Yordano kuti akabatizidwe. Iye anali atayenda kuchokera ku Galileya kupita kumene Yohane Mbatizi anali kulalikira ndi kubatiza. Yesu, ali ndi zaka zokwana 30, anali wokonzeka kuyamba utumiki wake ndi kukwaniritsa cholinga chimene anachokera chakumwamba ndikubwera pansi pano. Pamene Yesuyo amayendabe m'madzi muja, Yohane anayamba kudziona kuperewera ndipo anayamba kukana nati: "Ndiyenera ine kubatizidwa ndi Inu." Komabe, Mulungu anali atasankha Yohane kuti adzawulule Mesiya ku dziko lonse.

Yohane Mbatizi anamugwira Yesu namulowetsa m'madzi muja mpaka yense anamira. Pamene amatuluka mu mtsinjemo, madzi amayenderera pa nkhopo ya Khristu, ndipo kumwamba kunatsekuka. Mzimu wa Mulungu anatsika mwathupi ngati la nkhunda ndipo anatera pa Yesu. Liwu la Mulungu Atate linamveka kuchokera Kumwamba ndipo onse anamva kuti: "Uyu ndiye mwana wanga wokondedwa, mwa Iyeyu ndikondwera." Khamu la anthu linaima ndipo linali lozizwa ndi vumbulutso la Mulungu lodabwitsali. Yohane Mbatizi anachitira umboni za Yesu kuti "Mwana wa Mulungu ndi Yemweyu."

Chidzalo chonse cha Mulungu chinaonekera tsiku lija pa Mtsinje wa Yordano. Mulungu mmodzi mwa Atatu, monga anthu atatu osiyana, chinali chinthu chimene chinalongosoledwa bwino. Yesu Khristu ngakhale anali Mwana wa Mulungu, anabatizidwa ngati munthu. Mzimu Woyera ngati munthu anatsika monga

nkhunda. Atate ngati munthu analankhula kuchokera kumwamba. Mulungu Atate, Mwana ndi Mzimu Woyera akhala limodzi ngati anthu atatu komabe onsewa timawatchula kuti ndi Mulungu mmodzi.

Utatu wa Mulungu ndi chipunzitso chimene chimalongosola za chikhaldwe cha Mulungu. Chipunzitso chimene chimatanthauzira za mgwirizano wa anthu atatu—Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera—mu Umulungu. Mu zaka zapita, mutu umenewu wakhala gwero la mtsutso pa ziphunzitso zachikhristu. Ngakhale lero, pali Akhristu ambiri amene amakana kukhulupirika kwa Utatu wa Mulungu. Chipunzitso cha Utatu wa Mulungu chimanena kuti:

1. Pali Mulungu mmodzi yekha basi.
2. Mulungu akhala wamuyaya mwa anthu atatu osiyana.
3. Atate ndi Mulungu, Mwana ndi Mulungu, ndipo Mzimu Woyera ndi Mulungu.
4. Atate si Mwana, Mwana si Atate, Atate si Mzimu, etc.

Akulaukulu amene analipo usanachitike msonkhano wa pa Nicaea (chisanafike chaka cha 325 AD) adatsimikiza za umulungu wa Khristu ndipo amanena za "Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera." Mkulu wina wofunkira kwambiri mu mbiri ya mpingo dzina lake Tertullian, mchaka cha 215 AD, ndi amene anali woyamba kugwiritsa ntchito mau akuti "Utatu wa Mulungu" pofuna kulongosola za ubale wa Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera kuti ndi "achikhaldwe chimodzi—koma si munthu mmodzi."

(Yapitirira pa tsamba 2)



**Chidzalo chonse  
cha Mulungu  
chinaonekera tsiku  
lija pa Mtsinje wa  
Yordano. Mulungu  
mmodzi mwa Atatu,  
monga anthu atatu  
osiyana, chinali  
chinthu chimene  
chinalongosoledwa  
bwino.**

# ZIMENE BAIBULO

## LIMAPHUNZITSA ZA...

### Mau a Mulungu

2 Tim. 3:16-17; 2 Pet. 1:20-21; Mat. 24:35

### Ubale wa Chikondi

Mat. 22:37-40; Yoh. 14:21-23; 1 Yoh. 4:7-11

### Kulapa

Mach. 3:19; Mach. 17:30; 2 Akor. 7:10

### Kubadwa mwatsopano

Yoh. 3:3-7; 2 Akor. 5:17; Aro. 6:1-4;  
Aef. 2:1, 5-6

### Kupulumuka ku uchimo

1 Yoh. 5:18; Mat. 1:21; Yoh. 8:11

### Chidzalo cha Mzimu Woyeria

Mach. 19:2; Mach. 15:8-9; Mach. 1:8

### Chiyoero

Luk. 1:73-75; Aheb. 12:14; 1 Pet. 1:15-16;  
Tit. 2:11-12; Aro. 6:22

### Ufumu wa Mulungu

Luk. 17:20-21; Aro. 14:17; Yoh. 18:36

### Mpingo

Mach. 2:47; Aef. 4:4-6; 1 Akor. 12:12-13;  
Akol. 1:18

### Umodzi

Yoh. 17:20-23; Agal. 3:28; Chiv. 18:2-4

### Maskaramenti

Mat. 28:19-20; Mat. 26:26-30;  
1 Akor. 11:23-27; Yoh. 13:14-17

### Machiritso

Luk. 4:18; Yes. 53:4-5; Yak. 5:13-16

### Chiyoero cha Banja

Mat. 19:5-6; Luk. 16:18; Aro. 7:2-3;  
1 Akor. 7:10-11

### Chikhaliwe cha pakati pa anthu ena

1 Tim. 2:9-10; 1 Akor. 11:14-15; Deut. 22:5

### Masiku omaliza

2 Pet. 3:7-12; Yoh. 5:28-29; 2 Akor. 5:10;  
Mat. 25:31-46

### Kukhala mwa mtendere

Luk. 6:27-29; Luk. 18:20

### Kupembedza

Yoh. 4:23-24; Aef. 5:19; 2 Akor. 3:17

### Kulalikira Uthenga Wabwino

Mrk. 16:15

(Kuchokera pa tsamba 1)

Panali mtsutso wokhudzana ndi umulungu komanso kusandulika munthu kwa Khristu mu mpingo woyamba. Mzaka za ma 300-400AD, munthu wina dzina lake Arius analimbikitsa za chipunzitso chabodza chakuti Atate analipo Mwana asanakhalepo. Iye ananena kuti Khristu sanali Mulungu mwachibadwidwe ndiponso sanali wamuyaya. Chi Arianism chimagwiritsitsa mfundo yakuti Khristu anali woposa zolengedwa zonse. Chipunzitso chimenechi chinayamba kufala mwachangu ngati moto wakutchire.

Pamene Constantine anakhala pa mpando wa ufumu ndi kupangitsa kuti Chikhristu chikhale chipembedzo cha ku Roma, iye anayitanitsa Msonkhano Woyamba wa ku Nicaea

m'chaka cha 325 AD kuti akonze za

kusagwirizana pa chipunzitso

chokhudza chikhaliwe cha

Khristu ndiponso kufotokozerwa

ubale wa Mwana kwa Atate.

Athanasius wa ku Alexandria

analii mtsogoleri wa iwo amene

amalimbikitsa za umulungu

wa Khristu komanso kuti

Iye ndi wofanana ndi Atate.

Ngakhale kuti panthawi

imeneyi mumpingo panali anthu

amene amasiya chikhulupiro,

ambiri mwa mabishopu amene

analipo panthawiyi anatsutsana

ndi chipunzitso chonyenga cha

Arius ndipo anatsimikizango choonadi

cha Baibulo kuti Khristu anali Mulungu, wamuyaya, komanso gawo

la Umulungu. Bwalo la ku Nicaea lidavomereza chikhulupiro cha

pa Nicaea chimene chinalongosola kuti Khristu ndiye "Mulungu wa Mulungu, Kuwala kwa Kuwala, Mulungu weniweni wa Mulungu weniweni, wobadwa yekha, osalengedwa, wa chikhaliwe chimodzi ndi Atate."

Maziko a chikhulupiro cha Chikhristu ndiwo akuti pali Mulungu mmodzi amene ali pa anthu atatu. Ngati tingakane umulungu wa Khristu, palibe chiombolo kuchokera ku uchimo popeza mwazi wake sukadakhala ndi mphamvu kuposa uwo wa ng'ombe ndi mbuzi. Tithokoze Mulungu Atate amene anatuma Mwana wake Yesu ku dziko lino kuti adzafera machimo athu kuti ife tikoza kupulumutsidwa ndi kukhala kachisi wakuti Mzimu Woyeria akhale mkaati mwa ife.

—mws

## KODI MUMAKONDA ZIMENE MUMAWERENGA?

Papita zaka 5 tsopano tikulemba kalata ya *Uthenga Wabwino* ndipo zonse zasungidwa pa intaneti. Kuti muone pitani pa [www.thegospeltruth.org](http://www.thegospeltruth.org)

pamene mupezapo ziphunzitso zosiyanasiyana zoposa 20.

Gospel Truth ndi kalata imene imasindikizidwa miyezi itatu illyonse ndi a mpingo wa Church of God pofuna kulangiza ndi kulimbikitsa zoonadi zopezeka mu Baibulo. Kuti mudziwe zambiri werengani pa intaneti popita pa [www.thegospeltruth.org](http://www.thegospeltruth.org) ndipo muyankhe email imene mulandire ngati mukufuna kuti mudzilandira nawo kalatayi. Kalata ya Gospel Truth imasindikizidwa mu maiko ambiri kuti iperekedwe kwalere m'dzikomo ndipo chuma chohandizira ntchitoyi chimachokera ku ndalamu zimene ena amapereka mwafulu. Ngati mukufuna lisiti yoonetsa zimene mwapereka, tidzakupatsani.

—Editor, Michael Smith

Gospel Truth, P.O. Box 2042, Nixa, MO 65714 USA

[editor@thegospeltruth.org](mailto:editor@thegospeltruth.org)

# Mau a Mkonzi



*Pakuti mwa Iye [Mulungu] tikhala ndi moyo ndi kuyendayenda, ndi kupeza mkhaliidwe wathu; monga enanso aakuimba anu ati, Pakuti ifenso tili mbadwa zake. Popeza tsono tili mbadwa za Mulungu, sitiyanera kulingalira kuti umulungu uli wofanafana ndi golide, kapena siliva, kapena mwala, wolocha ndi luso ndi zolingalira za anthu. — Machitidwe 17:28-29*

Ife tili ndi mpweya komanso mphamvu chifukwa cha Mulungu yekha basi, popeza Iye ndiye kasupe wa Moyo. Ndi chifukwa cha Mulungu yekha basi kuti tili ndi mtendere, chipulumutso, ndi chiyembekezo cha moyo wosatha. Pokhala ana a Mulungu—anthu amoyo ndi anzeru—sitiyanera kupeputsa Umulungu kukhala chinthu chosapuma chimene chinalengedwa ndi munthu koma tizindikire kuti Mulungu ndi woposa chilengedwe chonse ndipo tiyenera kumupembedza.

Ulendo uno, ndikamba za mutu wa Utatu wa Mulungu ndipo ndifufuza malemba kuti akuti chiyani pa chipunzitso cha Utatu wa Mulungu. Ndadalitsika kwambiri pamene chikhalidwe cha Mulungu chakkala chikuvumbulutsidwa kwa ine kudzera mu kuphunzira kwa Mau a Mulungu. Ngakhale kuti ndikovuta kumvetsetsa mutu wa Utatu wa Mulungu ndipo zitsanzo ndi zithunzi zimene zimaperekedwa pofuna kulongosolera za mutuwu ndi zosakwanira, choonadi chake ndi chofunikira kwambiri kuti timvetsetse cholinga cha Mulungu komanso zimene iye anawakonzera anthu. Monga wolemba wina ananena kuti: "Ngati mukufuna kufotokozenza za Utatu wa Mulungu, mungochitapo misala. Komanso mukakana kuti sizoona, mungotayapo moyo wanu womwe."

Taganizirani zimene analemba F. G. Smith pa mutuwu mu buku lake lotchedwa *What the Bible Teaches*:

Kwa ambiri, chipunzitso ichi cha Utatu wa Mulungu chimaoneka ngati chinthu chosafunikira, koma zenizeni zake nzakuti izi sizoona. Ngati Khristu, ndi ungwiro wake wodabwitsa, sangakhale Mulungu weniweni, ndiye kuti mmalo molunzanitsa anthu ndi Mulungu, Iye wangokwaniritsa kutiwululira ife za phompho losadumphika limene lili pakati ndi ife ndi Wakumwambayo. Koma ngati Iye alidi "Mulungu woonekera mwa thupi" ndicholina chofuna kutembenza munthu wochimwa kuti akhale mu chifanizo chake, pamene po tili ndi chitsimikizo chakuti tili nako kulumikizana ndi kuyanjana kwauzimu ndiponso kwabwino ndi Atate wa kumwamba.

Popeza chikhalidwe chenicheni cha Umulungu chimaonekera kumwamba komanso kuposa kuganiza kwathu koperewera, tsinde la mmene tingapereke ulema kwa Mulungu likhazikike pa zimene zaululidwa kwa ife kudzera m'Malemba Oyera. Ndipo pamene tiwagwiritsa ntchito mwachindunji, tipeza kuti ndi kovuta kusemaphana ndi chipunzitso cha Utatu wa Mulungu umene umaphunzitsidwa ndipo sitidzaononga zochuluka zimene zinalembewda pa mutuwu. (p. 45)

Pemphero langa ndilo lakuti amene akuwerenga avomere kuti Mau a Mulungu ndi osavuta kuwalandira ndipo iwo amalongosola chikhalidwe cha Mulungu. Ndi dalitso lalikulu kuzindikira Mulungu mmodzi mwa atatu amene amagwira ntchito ndi kuchitachita mu miyoyo yathu ya tsiku ndi tsiku.

Michael W. Smith  
October 2017

Zambiri Zili pa  
**INTANETI**

Mukafuna kutipeza

pa intaneti, mulembe

[www.thegospeltruth.org](http://www.thegospeltruth.org)

kuti mudzilandira makalata

athu kabenanso kuti

muone makalata akale.

**"CHIFUKWA CHAKE WAMKULU NDI INU YEHAVA MULUNGU, PAKUTI PALIBE WINA WOFANANA NDI INU, PALIBE MULUNGU WINANSO KOMA INU, MONGA MWA ZONSE TINAZIMVA NDI MAKUTU ATHU."**

**—2 SAMUELE 7:22**

# Kalozera posanthula Mau a Mulungu

## Mutu: Utatu wa Mulungu

**Kuwerenga Malemba:** Pakuti pali atatu akuchita umboni, Mzimu, ndi madzi, ndi mwazi; ndipo iwo atatu ali mmodzi. —1 Yohane 5:7-8

**Kunena mwachidule:** Pali Mulungu mmodzi yekha basi, amene akhala wamuyaya chikhalidwe mu umodzi wa anthu atatu—Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera. Ngakhale kuti anthu awa ali osiyana kwa wina ndi mnzake, iwo paokha komanso mu ntchito zawo, iwo ali amodzi ndi a chikhalidwe chimodzi.

**Kumasulira:** Mau a mchingerezi akuti Trinity amene amanena za Utatu wa Mulungu akuchokera ku mau awiri “tri” ndi “unity,” ndipo amalongosola za kukhala atatu komabe ali mmodzi. Ndi mau amene timawagwiritsa ntchito pa chipunzitso cha zauzimu pofuna kunena kuti Mulungu Atate, Mulungu Mwana, ndi Mulungu Mzimu Woyera ali anthu atatu osiyana okhalira limodzi, amuyaya komabe ali Mulungu mmodzi.

### I. Mulungu mmodzi

- A. Deuteronomo 6:4 Yehova Mulungu wathu ndi Yehova mmodzi. (Marko 12:29)
- B. 1 Akorinto 8:4-6 Palibenso wina Mulungu koma mmodzi basi.
- C. Agalatiya 3:20 Mulungu ndi mmodzi.
- D. 1 Timoteo 2:5 Pali Mulungu mmodzi.

### II. Mulungu Atate

- A. 2 Petro 1:17 Analandira kuchokera kwa Mulungu Atate.
- B. Aefeso 5:20 Kuthokoza Mulungu ndi Atate.
- C. Yohane 6:27 Kwa iye amene Mulungu Atate anamlembira chizindikiro.
- D. Aroma 1:7 Chisomo ndi mtendere kuchokera kwa Mulungu Atate wathu.
- E. 1 Petro 1:2 Mulungu Atate anatidziwa kale.

### III. Mulungu Mwana

- A. Yohane 20:28 Ambuye wanga ndi Mulungu wanga.
- B. Ahebri 1:8 Kwa Mwana Iye anati, Mpando wanu wachifumu, Mulungu, ufikira ku nthawi za nthawi.
- C. Yohane 1:1, 14 Mauwo [Yesu] anali Mulungu.
- D. 1 Timoteo 3:16 Mulungu anadzionetsera mu thupi.
- E. Afilipi 2:5-6 Khristu Yesu mu chikhalidwe cha Mulungu.
- F. Mateyu 1:23 Yesu mwanayo ndiye Emmanuel kapena kuti “Mulungu ali nafe.”
- G. Yesaya 9:6 Mwanayo amatchedwa kuti “Mulungu Wamphamu.”
- H. Akolose 2:9 Mwa Iye chikhala chidzalo chonse cha Umulungu m’thupi.
- I. Akolose 1:15-16 Khristu ndiye chifanizo cha Mulungu. Zinthu zonse zinalengedwa ndi Iye.

### IV. Mulungu Mzimu Woyera

- A. Genesis 1:1-2 Mzimu Woyera anali wolenga.
- B. Machitidwe 5:3-4 Kunamiza Mzimu Woyera ndi chimodzimodzi kunamiza Mulungu.
- C. 1 Akorinto 3:16 Mzimu wa Mulungu amakhala mu kachisi wa Mulungu.

- D. Aroma 8:14 Iwo amene atsogozedwa ndi Mzimu ali ana a Mulungu.

### V. Utatu wa Mulungu ukuwululidwa

- A. Mateyu 3:16-17 Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera onse analipo ndithu pa ubatizo wa Khristu.
- B. Mateyu 28:19 Batizani mu dzina la Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera.
- C. Luka 1:30-35 Anthu atatu a pa Mulungu polingalira za kuikidwa mmimba kwa Khristu.
- D. Machitidwe 7:54-56 Stefano, wodzazidwa ndi Mzimu Woyera, anaona Yesu ataimirira pambali pa Mulungu.
- E. Yohane 14:26 Utatu wa Mulungu ukuwonetedredwa. (Yohane 15:26)
- F. 1 Akorinto 12:4-6 Mzimu yemweyo, Ambuye yemweyo, ndi Mulungu yemweyo.
- G. 2 Akorinto 13:14 Magawo atatu a Mulungu akutchulidwa momveka bwino.
- H. Aefeso 4:4-6 Mzimu mmodzi, Ambuye mmodzi, ndi Atate.


### VI. Umodzi wa utatu wa Mulungu

- A. Genesis 1:26-27 Munthu analengedwa mu chifanizo ndi chikhalidwe cha Mulungu mmodzi mwa Atatu. (Genesis 3:22)
- B. 1 Yohane 5:7 Atate, Mau [Yesu], ndi Mzimu Woyera ali amodzi.
- C. Yohane 10:30; 17:11, 22 Yesu ndi Atate amodzi.
- D. Yohane 10:38 Atate ali mwa Yesu ndipo Yesu ali mwa Atate.
- E. Yohane 12:44 Kukhulupirira mwa Yesu ndiko kukhulupirira mwa Atate.
- F. Yohane 14:8-11 Kuona Khristu ndiko kuona Atate.

**Kumaliza:** Yesu anayankha, kuti, La m’tsogolo ndili, Mvera, Israele; Ambuye Mulungu wathu, Ambuye ndiye mmodzi. —Marko 12:29

# UTATU WA MULUNGU

Baibulo limaphunzitsa momveka bwino kuti pali Mulungu mmodzi woona ndi wamoyo amene analenga dziko lonse—lye ndi wamuyaya, wamphamu zonse, wosasinthika, wokhala ndi mphamu zopanda malire, wanzeru, wachilungamo ndi woyera. Pa nthawi yomweyo, ilo limaphunzitsanso kuti Atate ndi Mulungu, nayenso Yesu ndi Mulungu, komanso Mzimu Woyera ndi Mulungu. Ubale wa Mulungu mmodzi mwa anthu atatu osiyana amene ali ndi umulungu umadziwika ndi mau akuti Utatu wa Mulungu.



Mfundu iyi ya Utatu wa Mulungu ndi mfundu yosamvetseteka ndipo ikhoza kukhala yovuta kuimvetsetsa kwambiri ndi kuizindikira. Mulungu ndi woposa anthufe kwambiri ndipo maganizo athu paokha sangathe kuzindikira ndi kumvetsetsa zozama ndi umphumphu wa Mulungu. Pa nthawi yomweyo, nkofunikira kumvetsetsa zimene Baibulo limanena pa mutuwo popeza chipulumutso ndiponso kusunga kwa moyo kumatengera zoonadi ndiponso zenizeni za utatu wa Mulungu.

## Mulungu ndi Mulungu mmodzi

Pamene Yesu anafunsidwa za lamulo loposa onse, lye anayankha nati, "Mvera, Israele; Ambuye Mulungu wathu, Ambuye ndiye mmodzi" (Marko 12:29). Tinganenenso kuti, "Yehova Mulungu wathu, Yehova ndiye mmodzi." Mitundu ina imapembedza milungu yambiri, koma Mulungu wa Ayuda anali mmodzi. Tikatenga mau a pa Deuteronomo 6:4, Yesu anatsindikanso choonadi chakuti pali Mulungu mmodzi yekha amene ali oona. Mulungu wa mu Chipangano Chakale ndi Mulungu wa mu Chipangano Chatsopano. Kupembedza Mulungu mmodzi ndi mfundu yofunikira ya Mau a Mulungu ndipo chipunxitso chonena za Mulungu chisamakhale chokhulupirira milungu itatu yokhalira pamodzi kapena milungu itatu yosiyana. Paulo ananena pa 1 Akorinto 8:4 kuti "palibe Mulungu koma mmodzi." Choondi chimenechi chikutsimikizidwanso pa Agalatiya 3:20, "Mulungu ndi mmodzi" ndi pa 1 Timoteo 2:5, "Pali Mulungu mmodzi."

## Mulungu ndi mmodzi mwa Atatu

Mulungu mmodziyo ndi Mulungu mmodzi mwa Atatu. Mu Umulungu muli Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera. "Pakuti pali atatu akuchita umboni, Mzimu, ndi madzi, ndi mwazi; ndipo iwo atatu ali mmodzi." (1 Yohane 5:7). Mu Malemba pali kutsindika komveka bwino kwa utatu wa Mulungu ndiponso za umodzi wa chikhaliwe chaumulungu cha Mulungu. Munthu

(Yapitirira pa tsamba 6)

**"Atate, Mwana, ndi  
Mzimu Woyera  
ndi anthu atatu  
amene akhala  
mu mgwirizano  
wangwiwo  
ngati Mulungu  
mmodzi. Iwowa si  
maina a magawo  
osiyanasiyana a  
Mulungu, popeza  
iwowa ali Mulungu,  
ndipo Mulungu  
ndi mmodzi"**



(Kuchokera pa tsamba 5)

aliyense mwa Atatuwo amadziwika kuti ndi Mulungu mu Malemba. Iwo si milungu itatu, koma onse pamodzi ndiye Mulungu mmodzi. Gawo lililonse la pa Mulungu limadziwika mwapaderadera mu Baibulo—Mulungu Atate, Mulungu Mwana, ndi Mulungu Mzimu Woyera.

### **Mulungu Atate**

Mau akuti Mulungu Atate amapezeka mu mavesi ambiri. Yesu ananena za "Mulungu Atate" mu Yohane 6:27. Paulo polembera ku mpingo wa ku Roma anati: "Chisomo chikhale ndinu ndi mtendere wa kwa Mulungu Atate wathu" (Aroma 1:7). Petro ananena za Yesu kuti "Pakuti analandira kwa Mulungu Atate ulemu ndi ulemerero" (2 Petro 1:17). Iye anapitiriza kunena za "kudziwiratu kwa Mulungu Atate" (1 Petro 1:2). Mulungu Atate anali munthu payekha amene Khristu ndi atumwi anakamba za Iye.

### **Mulungu Mwana**

Chipangano Chakale ndi Chatsopano chimanena kambirimbiri zakuti Yesu Khristu anali Mulungu. Ngakhale kuti ambiri amakana za umulungu wa Khristu kapena kuphunzitsa kuti Iye anali gawo pa Mulungu. Mneneri Yesaya analemba kuti: "Pakuti kwa ife mwana wakhanda wabadwa, kwa ife mwana wamwamuna wapatsidwa...ndipo adzamutcha dzina lake Wodabwitsa, Wauphungu, Mulungu wamphamu" (Yesaya 9:6). Mngelo wa Ambuye anaonekera kwa Yosefe nalankhula zakuti Maria adzabala mwana wamwamuna "ndipo adzamutcha dzina lake, Imanuele. Ndilo losandulika, Mulungu nafe" (Mateyu 1:23). Mu mau okoma a pa Yohane 1:1, 14 akunena kuti, "Pachiyambi panali Mau [Yesu], ndipo Mau anali kwa Mulungu, ndipo Mau ndiye Mulungu....Ndipo Mau [Yesu] anasandulika thupi, nakhazikika pakati pa ife, (ndipo tinaona ulemerero wake, ulemerero wonga wa wobadwa yekha wa Atate,) wodzala ndi chisomo ndi choonadi." Iye analipo kuyambira

kalekale. "Koma ponena za Mwana, ati, Mpando wachifumu wanu, Mulungu, ufikira nthawi za nthawi" (Ahebri 1:8). Yesu, anatumidwa ndi Atate, anali Mulungu amene anasundika thupi pakati pathu (Aroma 9:5). "Ndipo povomerezeka, chinsinsi cha kuchitira Mulungu ulemu nchachikulu: Iye amene anaonekera m'thupi" (1 Timoteo 3:16). Pamene Tomasi anaona Yesu amene anali atapachikidwa masiku apita, iye anayankha "nati [kwa Yesu woukitsidwayo], Ambuye wanga, ndi Mulungu wanga" (Yohane 20:28). Yesu anali mu chifanizo ndi chikhaldwe cha Mulungu (Afilipi 2:5-6) ndipo "pakuti mwa Iye chikhalira chiddalo cha Umulungu m'thupi" (Akolose 2:9). Mosakayika konse, pali chitsimikizo chochuluka chocokera mu baibulo chakuti Yesu ndi wamuyaya ndiponso ali ndi umulungu.

### **Mulungu Mzimu Woyera**

Mzimu Woyera ndi gawo lachitatu la Utatu wa Mulungu. Ngakhale pakuyamba pa nthawi, Mzimu Woyera analipo ngati wolenga. "Pachiyambi Mulungu adalenga kumwamba ndi dziko lapansi. ....ndipo mzimu wa Mulungu unalinkufungatira pamwamba pa madzi" (Genesis 1:1-2). Mzimu Woyeraakuwululidwa ngati Mulungu pa Machitidwe 5:3-4. "Koma Petro anati, Ananiya, Satana anadzaza mtima wako chifukwa ninji kudzanyenga Mzimu Woyera. ...Sunanyenga anthu, komatu Mulungu." Kunamiza Mzimu Woyera ndiko kunamiza Mulungu. Gawo lina lotsimikiza za Mulungu Mzimu Woyera likupezeka pa 1 Akorinto 3:16: "Kodi simudziwa kuti muli Kachisi wa Mulungu, ndi kuti Mzimu wa Mulungu agonera mwa inu?" Kodi ndani akhala mu kachisi kapena malo okhalamo a Mulungu kupatula Mulungu Mwinilake? Ndi Mulungu Mzimu Woyera amene akhala mu akachisi a Mulungu a pansi pano. Mzimu Woyera, pokhala Mulungu, amaonetsa ulamuliro waumulungu pamene amaitana ndi kupereka mphatso kwa oyera mtima a Mulungu (Machitidwe 13:2). Umulungu wake

ukuvumbulutsidwa pa Aroma 8:14: "Pakuti onse amene atsogozedwa ndi Mzimu wa Mulungu, amenewo ali ana a Mulungu."

## Mmodzi mwa Atatu

Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera ndi anthu atatu amene akhala mu mgwirizano wangwiro ngati Mulungu mmodzi. Iwowa si maina a magawo osiyanasiyana a Mulungu, popeza iwowa ali Mulungu, ndipo Mulungu ndi mmodzi. Mu ndime zochuluka, tikupezamo chitsanzo koma kuululidwa kwa Utatu wao. Pamene mngele anaonekera kwa Maria monga akunenera pa Luka 1:30-35, uthenga wake unakhudza magawo onse a Utatu Woyera. Mulungu Atate amamufungatira iye ndipo Mzimu Woyera anabwera pa iye kuti akhoza kukhala ndi pakati pa Mwana wa Mulungu. Zimenezi zinaloseredwa kuti Ambuye Mulungu adzapereka kwa Mwanayo mpando wachifumu ndipo kuti Ufumu wake sudzatha.

## Unawululidwa pa ubatizo wa Yesu

Anthu onse atatu a pa Mulungu analipo mwa njira inayake pa nkhani ya ubatizo wa Yesu pa Mateyu 3:16-17. Mzimu Woyera anatsika ngati nkhunda natera pa thupi la Yesu ndipo Atate analankhula mau kuchokera kumwamba. Nzoonekeratu kuti awa anali atatu osiyanu ndipo zikuonetsa kulakwitsa kumene kulipo pa chiphunzitso chakuti Mulungu Atate ndi Yesu ndi munthu mmodzi yemweyo.

Yesu anaphunzitsa ophunzira ake kuti abatizidwe "m'dzina la Atate, ndi la Mwana, ndi la Mzimu Woyera" (Mateyu 28:19). Izi zikunena za magawo onse a Mulungu. Anthu onse atatu akuwululidwa pamene Yesu analankhula ndi ophunzira ake zokhudzana ndi kubwera kwa Mzimu Woyera. "Koma Nkhosweyo, Mzimu Woyera, amene Atate adzamtuma m'dzina langa [Yesu], Iye adzaphunzitsa inu zonse, nadzakumbutsa inu zinthu zonse zimene ndinanena kwa inu" (Yohane 14:26).

## Unawululidwa pa kuphedwa kwa Stefano

Umulungu unawululidwa kwa Stefano pamene iye amaponyedwa miyala mu Machitidwe 7:54-56. Iye anali wodzazidwa ndi Mzimu Woyera ndipo anayang'ana kumwamba naona Yesu ataimirira ku dzanja lamanja la Mulungu [Atate]. Baibulo limanena za mphatso zosiyansiyana, kalongosoledwe kake, ndi magwiridwe

ake antchito koma limaphunzitsa kuti ndi Mzimu yemweyo, Ambuye yemweyo, ndi Mulungu yemweyo (1 Akorinto 12:4-6). Aefeso 4:4-6 amaphunzitsa kuti pali Mzimu mmodzi, Ambuye mmodzi, Mulungu mmodzi ndi Atate wa onse. Mulungu mmodzi mwa atatu, pokhala anthu atatu osiyanu, amawululidwa ma malemba amenewa.

## Umodzi wa Utatu wa Mulungu

Ngakhale kuti pa Utatu wa Mulungu pali atatu, koma Mulungu ndi mmodzi. Ngati mmodzi mwa atatu atachotsedwa, sipangakhalepo Mulungu. Ili ndi gawo la chinsinsi ndi chilungamo cha Mulungu chimene sitingachimvetse, popeza izi sizingasiyanitsidwe. Umodzi wa Utatu wa Mulungu ukuperekedwango ngati chitsanzo mu ndime zambiri za mu Baibulo. Pa Genesis 1:26 akuti, "Ndipo anati Mulungu, Tipange munthu m'chifanizo chathu, monga mwa chikhaldwe chathu". Taonani kuti Mulungu akutchulidwa ngati ambiri amene akunena kuti "ife" ndiponiso "chifanizo chathu." Izi zikuonetsa kupeze ka Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyera. Pa Genesis 1:27 akunena kuti "Mulungu ndipo adalenga munthu m'chifanizo chake." Tsopano tiona za umodzi wa Mulungu.

Yesu ananena mmalo angapo za mgwirizano wake ndi umodzi wake ndi Atate. "Ine ndi Atate ndife amodzi" (Yohane 10:30). "Atate ali mwa Ine, ndi Ine mwa Atate" (Yohane 10:38). Iye anapempherera umodzi wa ophunzira ake kuti iwo akhale amodzi "monga Ife tili mmodzi" (Yohane 17:11, 22). Yesu ananena pa Yohane 12:44, "Koma Yesu anafuula nati, Iye wokhulupirira Ine, sakhalupirira Ine, koma Iye wondituma Ine [Atate]. Filipo anafunsa Yesu kuti Iye awaonetse iwo Atate. Yesu anayankha popena kuti: "Iye amene wandiona Ine waona Atate; unena iwe bwanji, Mutionetsere Atate? Sukhulupirira kodi kuti ndili Ine mwa Atate, ndi Atate ali mwa Ine? Mau amene ndinena Ine kwa inu sindilankhula kwa Ine ndekha; koma Atate wokhala mwa Ine achita ntchito zake. Khulupirirani Ine, kuti Ine ndili mwa Atate ndi Atate ali mwa Ine" (Yohane 14:8-11).

(Yapitirira pa tsamba 8)



"Ngakhale kuti pa Utatu wa Mulungu pali atatu, koma Mulungu ndi mmodzi. Ngati mmodzi mwa atatu atachotsedwa, sipangakhalepo Mulungu. Ili ndi gawo la chinsinsi ndi chilungamo cha Mulungu chimene sitingachimvetse, popeza izi sizingasiyanitsidwe."


## Chipunzitso chomveka cha Mau a Mulungu

Chipunzitso ichi cha pa Mulungu, cha Utatu Woyerera, chimanenedwa momveka bwino mu Mau a Mulungu, ngakhale pali magawo ena amene ali ovuta kuwamvetsa. Zinthu zomwe ndi zosamveka bwino kuchokera m'Malembo zimakhala zosafunikira, ndipo mtsutso wa zinthu zimene siziphunzitsidwa mu Mau ukhoza kukhala wosapindulitsa. Ngati wina akana zoota zenizeni zokhudza chipunzitso cha Utatu Woyerera, akhoza kukana umulungu wa Mwana wa Mulungu kapena mphamvu ya umulungu ndiponso kuthekera kumene Mzimu Woyerera amapereka. Pali Mulungu mmodzi. Pali anthu atatu okhala ndi umulungu: Mulungu Atate, Mulungu Mwana, ndi Mulungu Mzimu Woyerera. Onse atatuwa ndi Mulungu mmodzi wachikhaliire kuyambira nthawi zosayamba. Akhristu akondwere ndi kulemekeza Mulunguyu amene wachita ndipo akupitiriza kuchita zinthu zazikulu mmalo mwa ana ake.

"Ha! Kuya kwake kwa kulemera ndi kwa nzeru ndi kwa kudziwa kwake kwa Mulungu! Osasanthulikadi maweruzo ake, ndi njira zake nzosalondoleka!... Chifukwa zinthu zonse zichokera kwa Iye, zichitika mwa Iye, ndi kufikira kwa Iye. Kwa Iyeyo ukhale ulemerero kunthawi zonse. Amen" (Aroma 11:33, 36). Tzikulambilani inu Mulungu—Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyerera.

—mws

# MAUDINDO OSIYANA A UTATU WA MULUNGU



**"ATATE AMAPANGA DONGOSOLO,  
YESU KHIRSTU AMAKWANIRITSA DONGOSOLOLO,  
NDIPO MZIMU WOYERA AMAONETSETSA KUTI DONGOSOLOLO LAYENDA BWINO."**

Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyerera pamodzi amagwirizana ngati Mulungu ndipo amagwira ntchito mwaumodzi kuyambira kumwamba ngakhalenso m'miyoyo ya anthu.

Ngakhale kuti onse atatu a pa umulungu ali ndi cholina chimodzi, ndipo ali ndi chikhalidwe komanso machitidwe ofanana, aliyense wa mu Utatu wa Mulungu ali ndi ntchito komanso maudindo apaderadera amene amachita.

Mmodzi mwa olemba mabuku amaumbwa mkota pa za maudindo a aliyense wa mu Utatu wa Mulungu motere: "Atate amapanga dongosolo, Yesu Khristu amakwaniritsa dongosololo, ndipo Mzimu Woyerera amaonetsetsa kuti dongosololo layenda bwino."

Mulungu Atate ndi chikondi. Iye ndi gwero komanso amene anapanga dongosolo lonse la chipulumutso.

Ndi Atate amene anatuma Mwana wake kuti adzakwaniritse dongosolo lake lowombola mtundu wa anthu.

Pofuna kumvera Atate, Yesu anatenga maonekedwe a thupi nafa pa mtanda kuti kudzera mu mwazi wake dziko lonse tikapulutsidwe ku uchimo. Yesu analumikiza cholekanitsa chimene chinali pakati pa Atate ndi mtundu wa anthu ndipo Iye ndi Mkulu wa ansembe komanso mkhalapakati wa anthu ake. Iye ndi mpulumutsi wa dziko ndi mutu wa mpingo.

Mzimu Woyerera, anatumizidwa kuchoka kwa Atate, ndipo amatsutsa uchimo, kuphunzitsa, kutsogolera ndi kutonthoza. Iye amayeretsa ndipo amakhala m'mitima ya anthu a Mulungu. Mzimu amapereka mphamvu ndi kupangitsa kuti anthu adzichita molingana ndi chifuniro cha Atate.

"Chisomo cha Ambuye Yesu Khristu, ndi chikondi cha Mulungu, ndi chiyanjano cha Mzimu Woyerera zikhale ndi inu nonse. Amen."

—2 Akorinto 13:14



# ZIKHALIDWE ZA MULUNGU

*Chaputala choyamba cha mu Baibulo chimayamba ndi mau akuti "Pachiyambi Mulungu...."*

*Mau amaulula kwa mtundu wa anthu za zikhalidwe ndi mkhalidwe wa Mulungu Mwini zimene anasankha kuti akhoza kugawana nave. Lingaliro lake, chifuniro chake, maweruzo ake amawunikira ndi kutipatsa cholinga pa moyo. Moyo umakhala wodzaza ndi wolemerera pamene tiphunzira ndi kumvetsetsa zambiri za khalidwe la Mulungu.*

# MULUNGU NDI...

## Wopanda thupi

Mulungu alibe thupi kapena chlichonse chimene tingathe kuchigwira.

"Mulungu ndiye mzimu." —Yohane 4:24

## Wokhala chikhaliire

Mulungu sanalengedwe ndipo sangafe. Iye akhali chikhaliire.

"Ndipo Mulungu anati kwa Mose, INE NDINE YEMWE NDILI INE." —Eksodo 3:14

## Wachikwanekwane

Mulungu safuna chinanso kunja kwa lye kuti akhale ndi moyo.

"Atate ali ndi moyo mwa lye yekha." —Yohane 5:26

## Wamuyaya

Mulungu alibe chiyambi ndipo sadzakhala ndi malekezero. Iye ndi wamuyaya ndipo nthawi yake ilibe malekezero.

"Asanabadwe mapiri, kapena musanalenge dziko lapansi, ndi lokhalamo anthu, inde, kuyambira nthawi yosayamba kufikira nthawi yosatha, Inu ndinu Mulungu." —Masalmo 90:2

## Wopanda malire

Mulungu sitingathe kumuyeza, alibe malekezero, ndipo alibe malire.

"Ambuye wathu ndi wamkulu ndi wa mphamu zambiri; nzeru yake njosatha." —Masalmo 147:5

## Mmodzi mwa Atatu

Mulungu anadziwulula yekha kwa mtundu wa anthu mwa anthu atatu—Atate, Mwana, Mzimu Woyeria.

Pakuti pali atatu akuchita umboni, Mzimu, ndi madzi, ndi mwazi." —1 Yohane 5:7-8

## Mmodzi

Mulungu ndi mmodzi ndi sangathe kugawidwa. Pali Mulungu mmodzi woona ndi wamoyo.

"Ambuye Mulungu wathu, Ambuye ndiye mmodzi." —Marko 12:29

## Waulamuliro wonse

Mulungu ali ndi ulamuliro ndi mphamu zoposa zonse ndipo amalamulira pa kena kalikonse.

"Pakuti Yehova ndiye Mulungu wamkulu; ndi mfumu yaikulu yoposa milungu yonse." —Masalmo 95:3

## Wansanje

Mulungu ndiye mwini kupembedzedwa ndipo tiyenera kutumikira zonse zimene zili zake.

"Pakuti musalambira mulungu wina; popeza Yehova dzina lake ndiye Wansanje, ali Mulungu wansanje." —Eksodo 34:14

## Wosasinta

Mulungu ndi wosasinta, wodalirika ndi wokhulupirika.

"Pakuti Ine Yehova sindisinthika." —Malaki 3:6



(Kuchokera pa tsamba 9)

## Opezeka paliponse

Mulungu ali paliponse ndi amapezeka paliponse.

“Kodi munthu angathe kubisala mobisika kuti ndisamuone iye? ... Kodi Ine sindidzala kumwamba ndi dziko lapansi? Ati Yehova.” —Yeremiya 23:24

## Wamphamvu zonse

Mulungu ali ndi mphamvu komanso ulamuliro wopanda malire.

“Mphamvu zonse zapatsidwa kwa Ine Kumwamba ndi pa dziko lapansi.” —Mateyu 28:18

## Wodziwa zonse

Mulungu amadziwa zinthu zonse ndipo ali ndi chidziwitso chake ndi changwiro. Iye amadziwa zammbuyo, zapano ndi zamtsogolo.

“Ndipo palibe cholebedwa chosaonekera pamaso pake, koma zonse zikhala za pambalambanda ndi zovundukuka pamaso pake pa lye amene tichita naye.” —Ahebri 4:13

## Wanzeru

Mulungu ali ndi chidziwitso chozama ndi amazindikira ndi kudziwa zimene zili zabwino kwambiri pa nyengo iliyonse.

“Lilemekezedwe dzina la Mulungu kunthawi za nthawi, pakuti nzeru ndi mphamvu zili zake.” —Daniele 2:20

## Chikondi

Mulungu amakhudzidwa kwambiri ndi ubwino wa anthu. Chikondi ndi chikhaldwe chimene chinganene khalidwe lenileni la Mulungu. Ndi choposa zimene timamva mthupi mwathu, ndi chinthu chimene timayenera kuchita.

“Ndipo ife tazindikira, ndipo takhulupirira chikondicho Mulungu ali nacho pa ife. Mulungu ndiye chikondi, ndipo iye amene akhala m’chikondi akhala mwa Mulungu, ndipo Mulungu akhala mwa iye.” —1 Yohane 4:16

## Woyer

Mulungu ndi wolungama ndi wangwiwo mu chiyero. Iye ali kutali ndi tchimo, choipa ndi chidetso chilichonse.

“Muzikhala oyera mtima, pakuti Ine ndine woyer mtima.” —1 Petro 1:16

## Wachilungamo

Mulungu amachita nefe mwa lamulo labwino ndi mosakondera molingana ndi chilungamo ndi chabwino.

“Chilungamo ndi chiweruzo ndiwo maziko a mpando wachifumu wanu.” —Masalmo 89:14

## Wabwino

Mulungu ndi wabwino, wokoma mtima ndi wodzaza ndi kukonderedwa ndi madalitso.

“Ubwino wa Mulungu ukubwezera kuti ulape.” —Aroma 2:4

## Wokhulupirika

Mulungu ndi wokhulupirika, wodalirika ndipo sanganame.

“Dziwani kuti Yehova Mulungu wanu ndiye Mulungu; ndiye Mulungu wokhulupirika.” —Deuteronomo 7:9

## Wachifundo

Mulungu is wokhululukira, wokhudzidwa ndi nkhwawa zathu ndi wachifundo.

“Yehova ndiye wa nsoni zokoma ndi wachisomo, wosakwiya msanga, ndi wa chifundo chochuluka.” —Masalmo 103:8

## Wachisomo

Mulungu ndi wachisomo ndipo amaperekwa mphatso kwa iwo amene ali wosayenera.

“Pakuti chaonekera chisomo cha Mulungu chakupulumutsa anthu onse.” —Tito 2:11

## Wosafanirizika

Mulungu sitingathe kumufanizira ndi china chilichonse. Alibe wofana naye ndipo ndi wangwiwo.

“Mudzandifanizira Ine ndi yani tsono, kuti ndilingane naye, ati Woyerayo.” —Yesaya 40:25

# Mafunso Mayankho ?

## Kodi umodzi wa umunthu ndi umulungu wa Yesu Khristu ndi wotani?

Yesu Khristu ndi munthu mmodzi amene ali ndi zikhaldwe ziwiri—cha mulungu ndi cha munthu. Umodzi wa umunthu ndi umulungu umalongsola za umodzi uwu wa umunthu ndi umulungu wa Khristu kuti ndi munthu mmodzi yemwego ndipo zonsezi zili mwa iyeyo. Yesu ndi Mulungu mu thupi. “Pachiyambi panali Mau [Yesu], ndipo Mau [Yesu] anali kwa Mulungu, ndipo Mau [Yesu] ndiye Mulungu. .... Ndipo Mau [Yesu] anasandulika thupi, nakhazikika pakati pa ife” (Yohane 1:1,14). Yesu anali ndi zikhaldwe ziwiri—Mulungu ndi munthu. Sanali gawo lina Mulungu ndi gawo lina munthu koma anali Mulungu wathunthu ndi munthunso wathunthu. Yesu sanataye umulungu wake koma anakhala pansi pano ngati Mulungu nakhanso ndi chikhaldwe cha umunthu.

## Kodi Utatu wa Mulungu tingaulongosole motani?

Pali zinthunzi zambiri zimene zakhala zikugwiritsidwa ntchito pofuna kufotokoza za Utatu wa Mulungu. Komabe zambiri mwa izo sizifikapo polongosola kwathunthu kuti Mulungu ndi mmodzi mwa atatu ndipo izozo tingazitenge ngati njira zosakwanira pofuna kupereka chithunzi cha chinsinsi cha Utatu wa Mulungu. Zikhzoa kukhala zoopsa kungolongosera mosakhala bwino chifukwa pamene ambiri alongosola chithunzi cha nkhanziyi, iwo ananena zinthu zabodza zokhudza Utatu wa Mulungu.

Dzira limagwiritsidwa nthawi zambiri pofuna kulongosolera za Utatu wa Mulungu. Dzira la nkuku limakhala ndi chigoba chakunja, chamkati choyera ndi chamkati kwambiri chachikasu ndipo zonsezi zimapanga dzira limodzi. Magawo onse atatuwa amapanga chinthu chimodzi. Komabe posiyana ndi Utatu wa Mulungu, chamkati chachikasu sidzira mwachokha komanso pachokha. Khristu ndi Mulungu wathunthu, komanso Mulungu ndi Atate, Mwana ndi Mzimu Woyer. Iwo onse ndi mmodzi kusiyana ndi magawo a dzira aja. Chimodzimodzinso, chipatso cha apple (apozi) chili ndi khungu, nyama yamkati ndi mbewu. Ichinso ngati dzira lija sихиканира pofuna kufotokoza mfundo yakuti pa Utatu wa Mulungu, aliyense waiwo payekha ndi munthu komabe ndi Mulungu.

Chitsanzo china chogwiritsidwa ntchito kawirikawiri chimakhudza madzi amene akhoza kukhala owuma gwaa ngati ayisi, omweka kapena kusambika ndipo ootcha ngati thunzi. Ngakhale amasinta chifukwa cha kuzizira kwambiri kapena kutentha kwambiri, komabe ndi madzi ndithu. Koma madziwo amakhala mu nyengo imodzi pa nthawi imodzi, mwachitsanzo, sauma gwaa, omwewo nkukhala osambika kapena ochita thunzi akuti ukhoza kumwera tiyi, pamene nthawi zonse Mulungu ali Atate, Mwana ndi Mzimu Woyer. Ngakhale kuti ayisi wouma gwaa akhoza kusunguka nasadzuka madzimadzi, Mwana sasinta kukhala Atate, kapena Atate kukhala Mzimu. etc.

Chitsanzo china chimene chimagwiritsidwa ntchito ndicho cha munthu amene ali atate, mwana ndi mwamuna wa mkazi wake nthawi yomwego, komabe iwo ndi munthu mmodzi yemwego. Izi zikhzoa kufotokoza bwino za ntchito za utatu wa Mulungu komabe siziwanitsa kulongosolera za kusiyana kwa anthu atatuwo a pa Umulungu

## Kodi ndi chifukwa chiyani Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyer amatengedwa ngati anthu?

Mulungu ndi utatu wa anthu: Atate, Mwana, ndi Mzimu Woyer. Iwo si munthu mmodzi yemwego koma pamodzi iwowa ndi Mulungu mmodzi. Atate si Mwana, kapena Mwana kapenango Mzimu, komabe aliyense wa iwowa ndi Mulungu. Izi zikulongosoledwa bwino pa chithunzi cha Utatu wa Mulungu chimene chili pa tsamba 5.

Iwowa si anthu ngati ife popeza sikuti onse ali ndi thupi ngati lathuli lokhala ndi nyama, koma kuti aliyense payekha amatha kuzindikira zinthu, kulanckhula, kukonda, kufuna kuchita. Zikhaldwe izi ndi za umunthu, ndi chifukwa chake tikugwiritsa mau amene timawagwiritsa nthawi zonse ponena za anthu.

Dr. Henry Morris ananena kuti chilengedwe cha dzikoli chimafafana ndi Utatu wa Mulungu. Chilengedwe chili ndi magawo atatu: zinthu zooneka ndi zogwirika, kumwamba ndi nthawi. Ngati tingachotse chimodzi cha izi, dzikolo silidzakhalapo. Izi zikuonetsa kuti pali kulumikizana kwakukulu pakati pa zitatuzi, gawo lililonse si gawo la thunthu monga mmene aliyense wa munthu pa Utatu ali Mulungu.

Zojambulajambula za masamu zimagwira ntchito yolongosola za Utatu Woyer. Mwachitsanzo, chojambula chokhala ndi makona atatu (triangle) chili ndi mbali zitatu zimene zimalumikizana kupanga chinthu chimodzi. Komabe izi siziwanira popeza mzere uliwonse pawokha si chojambulacho.

Ngakhale sikolakwika kuyesetsa kufotokoza za Utatu wa Mulungu, tidziwe kuti tkhoza kuphophonya. Zithunzi zonse ndi zolakwika ndipo sizilongosola mokwanira za Utatu wa Mulungu, popeza Mulungu wopanda malireyo sangatheke kulongosoledwa ndi zinthu zooneka ndi zakutha. Chiphunzitso cha Utatu wa Mulungu ndi vumbulutso lochokera kwa Mulungu osati chimene anthu anangochiganizira mwa nzeru zawo.



KODI MUKUDZIWA?

Pali mipingo yosiyansiyana ya Chikhristu imene imakana chiphunzitso cha Utatu wa Mulungu. Ngakhale ilipo yochepa, koma mipingo ikuluikulu imene imakana za nkhaniyi ndi ya The Church of God of Latter-day Saints (Mormons) ndi a Mboni (Jehovah's Witnesses).

A Jehovah's Witnesses amamutenga Yesu ngati kuti anali ndi chiyambi ndiponso kuti iye ndi cholengedwa cha Mulungu. Iwo sakhulupirira kuti Mzimu Woyeria ndi munthu koma kuti ndi mphamvu chabe ya Mulungu. Chipembedzo cha chi Mormon chimaphunzitsa kuti Mulungu analenga Khristu ndiponso kuti Mulungu ndi bungwe la milungu itatu yosiyansiyana. Izi zikumveka ngati kupembedza milungu yambiri kusiyana ndi chiphunzitso cha Baibulo cha Mulungu mmodzi.



## NDIKUFUNA NDIONE YESU YEKHA BASI

*Ndipo iwo, pokweza maso ao sanaone munthu, koma Yesu yekha. —Mateyu 17:8*

Yesu, pa phiri paja pamene anasinha maonekedwe, anayanjana ndi Mose ndi Eliya—Mose amaimira lamulo, pamene Eliya anaimira aneneri ndipo Yesu anaimira nyengo yatsopano ya chisomo. Podabwitsika ndi posangalala, Petro anadzipereka kuti apanga misasa itatu, umodzi wa aliyense wa iwo. Mtambo wowala unawaphimba iwo ndipo Atate analankhula: “Uyu ndiye Mwana wanga wokondedwa, mwa iyeyu ndikondwera, mverani lye” (v5). Chifukwa cha mantha, ophunzira aja anagwa nkhope zaho pansi. Pamene anakweza maso awo, sanaonenso munthu wina kupatulapo Yesu basi.



Pali magulu ambiri, mabungwe, mautumiki ndi anthu ochuluka amene amafuna kupeze ka kwathu komanso kudzipereka kwathu kwa iwo. Ngakhale kuti pali mabungwe ndi mautumiki abwino komanso odalirika, Khristu yekha, pamodzi ndi Atate, akhale amene ife tidzimpembedza ndi kumutumikira.

Tisasunthike kuti timtumikire Yesu chifukwa cha lamulo kapena aneneri koma chifukwa cha Khristu Mwini. Kaya ndi mu nthawi zabwino kapena zovuta, tiyenera kulimbkitsidwa ndi masomphenya akuti tisaone wina aliyense koma Yesu yekha basi. Mu dziko lino limene lili ndi mau osiyansiyana, makutu athu akufunika kumvera ku liwu limodzi la Mwana of Mulungu.

Pamene tikhazika maso athu pa anthu ndi zinthu, tidzakhumudwa ndi kufooketsedwa. Asilikali anzanga a Khristu, ikani maso anu pa Yesu. Muloleni Iye akhale chimene chikufulumizani kugwira ntchito ndi kutumikira, popeza lye ndi amene adzakhale wokhulupirika kukusamalirani mpaka mudzapambane. Monga nyimboyo inena kuti: “Ndikufuna ndione Yesu yekha basi.”

—mws

CHIYERO CHA KWA AMBUYE

Kuti Mutipeze  
The Gospel Truth  
P. O. Box 2042  
Nixa, MO 65714  
USA

Email:  
[editor@thegospeltruth.org](mailto:editor@thegospeltruth.org)